# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

**Za zimene zidzacitika**

1. Dziko lapansi lidzatha
2. Yesu adzabweranso
3. Zimene zidzacitika pamene Yesu abweranso
4. Ngati ndiyenera kumwalira
5. Kulemekeza Mulungu mpaka muyaya

Ndipo Iye wakukhala pa mpando wacifumu anati, Taonani, ndicita zonse zikhale zatsopano. Cibvumbulutso 21.5a

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

- ©Stephanos Zambia Trust –
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Dziko lapansi lidzatha

*Ndipo dziko ndi nchito ziri momwemo zidzatenthedwa – 2 Petro 3.10b*

**Kuwerenga**
2 Petro 3.10-13

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira kuti zinthu zonse ziri ndi ciyambi? Mau oyamba a m'Baibulo atiuza, 'Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi'. Kumwamba ndi dziko lapansi zidzakhalanso ndi kutha. Mulungu atiuza ici m'Baibulo.
Tsiku lina ophunzira a Yesu anayang'ana Kacisi wooneka bwino ku Yerusalemu. Iwo anati kwa Yesu, 'Bwerani kuona kukongola kwa Kacisi'.
Kacisi unamangidwa ndi miyala yaikulu yoyera ndipo unakongoletsedwa ndi golidi. Kunali mizati yaikuli ndi nsanja zazitali. Kunali makonde akulu ndi mipando kuti anthu akhalepo. O, zonse zinaoneka bwino kwambiri! Ophunzira anakonda Kacisi.
Yesu anayenda nao kuyang'ana mwadzumwadzu. Koma Iye anali wacisoni.
Yesu anati, 'Kodi muona izi zonse? Mverani, ndikuuzeni cinthu. Izi zonse zidzagwetsedwa. Sudzasiyidwa pano mwala umodzi pamwamba pa unzace'.
Ici cinacititsa cisoni ophunzira. Sanakonde kuganiza kuti tsiku lina Kacisi wooneka bwino udzagwetsedwa. Anaganiza kuti pamene Kacisi wagwetsedwa, ico cidzakhala kutha ndithu kwa dziko lapansi.
Koma zaka zocepa atapita Kumwamba Yesu, ankhondo a mfumu yoipa anagwetsa Kacisi.
Baibulo litiuza kuti dziko lidzatha pa tsiku lina. Zonse zimene tiona zidzafa. Zidzatenthedwa ndi moto.
Tikumva cisoni pamene tiganizira izi. Ndipo tiopa. Tsiku lija lidzakhala loipa kwambiri.
Baibulo limacha tsiku lija la kutha kwa dziko, *tsiku la Yehova lalikulu ndi loopsa*. Pa tsiku lija Ambuye Yesu adzatuma moto kucokera Kumwamba ndipo moto udzaononga zonse zimene ziri za uchimo. Moto udzathentha konse dziko lapansi. Zoipa zonse za Satana ndi za anthu zidzatenthedwanso. Ndipo Yesu adzakhala Ambuye wa zonse.
Tsiku lija, anthu onse adzadziwa kuti Mulungu ndi wamkulu kwambiri kupambana Satana. Onse adzaona Yesu ndi angelo ake. Ndipo onse adzagwadira Yesu. Pa tsiku lija adzadziwa kuti Iye ndi Mbuye wa ambuye ndi Mfumu wa mafumu ndithu.
Ndipo anthu oipa adzaopa. Adzapfuula. Tsiku lija ndi tsiku loipa kwambiri kuli iwo: tsiku la kulangidwa cifukwa ca macimo ao.
Koma ana a Mulungu sayenera konse kuopa. Iwo sadzalangidwa cifukwa ca macimo ao. Ndipo Mulungu adzawapulumutsa ku moto. Nthawi zonse Iye salola ciriconse kupwetekera ana ake okondedwa.
Ndipo Iye adzapanga Mwamba watsopano ndi dziko lapansi latsopano kuti anthu ake akhalako ndi kukhala moyo kumtumikira mpaka muyayaya.

**Kukambirana**
1. Cifukwa ciani Mulungu adzatentha dziko lonse lapansi?
2. Chulani zinthu zisanu za m'miyoyo yanu zimene zidzatenthedwa.
3. Kodi mukumva bwanji podziwa kuti zonse zidzatha?
4. Cifukwa ciani tsiku lija lichedwa *tsiku la Mulungu lalikulu ndi loopsa*?
5. Cifukwa ciani ana a Mulungu sayenera kuopa tsiku lotsiriza?
6. Kodi ndinu mwana wa Mulungu?
7. Kodi kudziwa kuti zonse zidzatha, kusinthitsa bwanji m'miyoyo yathu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, Pamene tiganiza za kutha kwa dziko lapansi tikumva mantha. Koma tikondwera pozindikira kuti tidzaona ukulu ndi ulemerero wanu. Tithandizeni kuwerengetsa miyoyo ndi mitima yathu pa maso panu. Tikupemphani m'dzina la Yesu, Amen.

**2. Yesu adzabweranso**

*Pakuti ife ndife anchito anzace a Mulungu – 1 Akorinto 3.9a*

**Kuwerenga**
Cibvumbulutso 1.4-7

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira kuti Yesu anapita Kumwamba? Anali pamwamba pa phiri pamodzi ndi ophunzira ake. Anakweza manja ake kudalitsa ophunzira ake. Ndipo kenaka anakwera ku Mwamba.
Ophunzira anadabwa. Kodi Iye anali kucita ciani? Iwo anamuona kupitiriza kukwera. Kenaka kunabwera mtambo. Mtambo unabisa Yesu kotero kuti iwo sanakhozebe kumuona.
Ophunzira anayang'anabe pamwamba. Anaganiza kuti mwina angaonenso Yesu ngati mtambo wacoka!
Ndipo kenaka, mwadzidzidzi kunali ena awiri pamodzi ndi ophunzira. Amunawo anabvala zobvala zoyera ndi zowala. Iwo anali angelo.
Angelo anati kwa ophunzira, 'Cifukwa ciani muimirira ndi kuyang'ana kumwamba? Yesu adzabweranso momwemo monga wapita Kumwamba. Adzabweranso pa mtambo'.
Pa kumvera ici, ophunzira anakondwera.
Koma iwo sanatsale pa phiri kuyembekezera Yesu kubweranso. O, iai. Anakumbukira zimene Yesu adawauza. Kunali nchito imene iwo anayenera kucita. Anayenera kuuza anthu ena nthano ya Yesu.
Zaka zambiri zinapitako kucokera pa nthawi ya kukwera kwa Yesu Kumwamba. Ndipo Iye sanabwerenso mpakana pano.
Koma Iye anati kuti adzabweranso. Ndipo angelo anati kuti Iye adzabweranso. Yesu amacita cimene alonjeza, monga mudziwa. Adzabwera ndithu.
Kodi adzabwera liti?
Iye asanapite Kumwamba, anauza ophunzira ake kuti dziko lonse lapansi liyenera kumvera Uthenga Wabwino. Anati kuti sadzabweranso mpaka mitundu yonse adziwa za Iye. Ndipo anatiuza kupita ndi kuuza mitundu yonse (anthu onse paliponse) za Iye.
Tiri ndi nchito kucita poyembekezera Yesu kubweranso. Nchito iyi ndi yofunikira koposa m'dziko lonse lapansi. Tiziuza nthano ya Yesu ndi cikondi cace. Tiziuza anthu ocimwa kupita kwa Yesu ndi kukhala oyeretsedwa. Tizikhala atumiki a Mulungu. Ndipo tiyenera kutuma atumiki a Mulungu.
Pamene nchito zonse zatha, Yesu adzabweranso. Adzabwera kutenga ana ake okondedwa kupita Kunyumba, kwa Atate. Pa nthawi iyo banja lonse la Mulungu lidzakhala pamodzi Kumwamba. Ici cidzakhala codabwitsa kwambiri!
Pamene tiganizirako izi, sitikhoza kuyembekeza. Tipempha, 'Ambuye Yesu, Idzani msanga!' Tiri kukonzekera kukomana naye. Ndipo tigwira nchito kusonkhanitsa ana a Mulungu ocokera m'maiko onse.
Pamene tizindikira momwe zinthu zidzakhala m'Mwamba, sitiganizira kwambiri zinthu za pa dziko lapansi. Koposa tiganizira zimene tikhoza kucitira Yesu ndiponso momwe tikhoza kudzikonzekera pa nthawi ya kubwera kwake.

**Kukambirana**
1. Kodi tidziwa bwanji kuti Yesu adzabweranso?
2. Kodi mukumva bwanji za kubweranso kwa Yesu?
3. Kodi tiyenera kucita ciani poyembekezera Yesu kubweranso?
4. Kodi ndi yani amene adziwa tsiku la kubweranso kwa Yesu kulingana ndi Mateyu 24.36?
5. Kodi mwakonzeka kukomana ndi Yesu woyera ndi wolungama?

**Citsanzo ca pemphero**
Tikuyamikani Ambuye Yesu Kristu, kuti mudzabweranso kutenga ana anu onse kukhala ndi Inu Kumwamba. Tikupemphani kuti mubwere msanga. Tithandizeni pamene tiuza mitundu yonse Uthenga wanu Wabwino. Tithandizeni kotero kuti sitifalitsa mabodza koma cabe cisomo, cikhululukiro ndi cifundo canu mwa Yesu Kristu. Tikupemphani izi m'dzina lanu, Amen.

### 3. Zimene zidzacitika pamene Yesu abweranso

*Pakuti Ambuye adzatika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu – 1 Atesalonika 4.16a*

**Kuwerenga**
1 Atesalonika 4.16-17

**Malongosoledwe**
Tsiku lina Yesu anauza nkhani ya mlimi amene anafesa mbeu m'munda mwake. Nchito yake atatsiriza, anacokapo ndiop mdani anabwera. Mdani anafesa mbeu zosafunika. Patapita nthawi mbeu zabwino zinayamba kukula. Koma mbeu zosafunika zinakulanso.
Anchito a mlimi anapita kuona munda. Anaona mbeu zosafunika pakati pa mbeu zabwino. Anathamanga kuuza mlimi. Iwo anamufunsa, 'Kodi simunafese mbeu zabwino?'
'Inde, ndinafesa mbeu zabwino', mlimi anati, 'Mdani anabwera nafesa mbeu zosafunika'.
Kenaka anchito anafuna kucotsa mbeu zosafunika. Koma mlimi anati, 'Iai, muzilole kukula pamodzi. Ngati mucotsa mbeu zosafunika, mwina mungacotsenso mbeu zabwino. Pa nthawi ya kukolola tidzacotsa mbeu zonse zosafunika ndipo tidzazitentha. Ndipo kenaka ndidzasonkhanitsa mbeu zabwino m'nkhokwe zanga.'
Ophunzira a Yesu anafunsa Iye citanthauzo ca nkhaniyo. Iwo anadziwa kuti nkhani inali fanizo: nkhani ya pa dziko lapansi imene iri ndi citanthauzo ca Kumwamba. Yesu anati, 'Munda ndi dziko lapansi. Mbeu zabwino ndizo ana a Mulungu. Mbeu zosafunika ndizo ana a Satana. Satana ndi mdani amene anawafesa. Iwo akula pamodzi tsono. Ana a Mulungu ndi a Satana akhala mbali ndi mbali.' Kukolola ndiko kutha kwa dziko lapansi ndipo anchito a kukolola ndiwo angelo. Mwana wa munthu (Yesu) adzatuma angelo ake. Iwo adzakhala monga akukolola amene anasonkhanitsa mbeu zosafunika kukazitentha. Koma Iye adzatenga ana a Ufumu kupita Kunyumba kukhala ndi Atate.
Pamene Yesu adzabweranso, anthu amene sanafune kumukonda ndi kumumvera, adzakhala wa cisoni kwambirimbiri. Mulungu adzawatuma ku mdima wakunja kumene Satana adzakhalako. Iwo adzakhala osakondwa mpaka muyaya. Ici ndi cacisoni.
Koma Mulungu adzatenga anthu ake Kumwamba. Ambuye Yesu adzabwera mwadzidzidzi pa mitambo ndipo angelo ake onse adzakhala naye. Kudzakhala mpfuu waukulu ndipo lipenga la Mulungu lidzamveka. Ndipo anthu onse a pa dziko lapansi adzaona Yesu.
Ngakhale anthu akufa a m'manda ndi a malo onse, adzaukitsidwa. Adzacoka m'manda mwao. Adzakhalanso moyo ndi kuona Yesu.
Pomwepo, iwo amene sanakonde Iye, adzamva mantha. Adzayesa kubisala. Koma iwo amene anamkonda ndi kumkondabe, adzakhala okondwera kwambirimbiri. Ndipo adzawatenga kukomana ndi Iye m'mitambo. Yesu adzatenga anthu ake kucokera ku malo onse, ngakhale kunyumba kapena ku sukulu. Iwo ocoka m'manda mwao, ngati anamkonda, adzapitanso ndi Iye. Adzakhala ndi matupi atsopano. Ana onse a Mulungu adzakhala ndi matupi atsopano: matupi a uzimu amene akonzeka kukhala Kumwamba.
Tsiku lija lidzakhala lodabwitsa kwambiri! Cifukwa cace tilakalaka ndi kupemphera tsiku iri kubwera msanga!

**Kukambirana**
1. Kodi kuli anthu otani pa dziko lapansi kulingana ndi fanizo limene Yesu anauza?
2. Kodi Yesu adzacita nao pamene abweranso?
3. Kodi muli m'gulu la mbeu zabwino kapena mbeu zosafunika?
4. Yesu sazengereza lonjezano la kubweranso kwake. M'2 Petro 3.9b tiwerenga, 'Komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa'. Kodi kulapa ndi kulandira Yesu kukhala Ambuye ndi Mpulumutsi kutanthauza ciani?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, Tsiku la kubweranso kwanu kudzakhala kodabwitsa kwambiri, pamene tidzakuonani. Tikupemphani kuti mutithandiza kudzikonzekera tsiku ndi tsiku kukomana ndi Inu, mwa mphamvu ya Iye amene anauka kwa akufa, mwa Iye amene ali ndi mphamvu zonse. Tikupemphani izi, m'dzina la Yesu, Amen.

## 4. Ngati ndiyenera kumwalira

*Tonse tidzasandulika – 1 Akorinto 15.51*

**Kuwerenga**
Afilipi 1.23

**Malongosoledwe**
Yesu ali kubwera ndipo kukomana ndi iye m'mitambo kudzakhala kodabwitsa. Koma mwina sitidzakhala ndi moyo mpaka tsiku la kubweranso kwake. Mwina muyenera kufa Iye asanabwere. Mwina ine ndiyenera kufa. Anthu okalamba afa. Nthawi zina anyamata ndi atsikana afa.
Petro, Yakobo, Yohane ndi mtumiki wamkulu Paulo, iwo onse analakalaka Yesu kubweranso. Anapempha kuti Iye adzabwera pamene iwo anali amoyo. Anaganiza kuti mwina adzakhala pa dziko lapansi kumvera pfuu ndi kumuona Yesu pobwera. Koma iwo anamwalira.
Mulungu anaganiza kuti zabwino zoposa zinali zotero. Ndipo mwina aganiza kuti cabwino koposa ndi kuti timwalira. Koma ici sicikhala cofunikira konse. Matupi athu adzaikidwa m'manda. Koma mizimu yathu idzapita Kumwamba! Matupi athu ndiwo monga nyumba cabe: nyumba ya mtima kapena mzimu. Mzimu wanu (ndiwo inudi) udzapita Kumwamba mosacedwa pokhaphoka ndinu m'modzi wa ana a Mulungu. Ndipo pamene Yesu adzabweranso adzaukitsa thupi lanu kuti lituruke m'manda ndipo adzalipangitsa kukhala nyumba yatsopano: thupi latsopano.
Anthu ambirimbiri a Mulungu anafa. Mizimu yao ali tsono Kumwamba, pamodzi ndi Yesu. Iwo akondwera kumeneko. Ndipo ali kuyembekezera tsiku lija lodabwitsa la Ambuye, pamene Yesu adzawapatsa matupi atsopano.
Pamene mtumiki Paulo anali mwamuna wokalamba, anaikida m'ndende cifukwa ca kulalikira za Yesu. Koma angakhale kukhala m'ndende, iye anacita zonse zimene akhoza kuuza nthano yodabwitsa ya cipulumutso. Ndipo analembera macalichi makalata kukumbutsa anthu kukhala oona kuli Yesu ndi kumukonda.
Tsiku lina Paulo analembera mnzake Timoteo kalata. Anauza Timoteo kuti nchito yake inali pafupi kutha. Anati kuti adzuwa kuti Mulungu adzabwera msanga kumtenga Kumwamba. Ndipo anati kuti anali ndi cilakolako cacikulu kupita. Paulo anafuna kumwalira.
Kodi mudziwa cifukwa ciani anafuna kumwalira?
Ici ndi cimene iye analemba m'kalata la calichi limodzi, 'Pokhala naco colakalaka ca kucoka kukhala ndi Kristu, ndiko kwabwino koposaposatu' (Afilipi 1.23).
O, inde tiloledwa kukondwera pano padziko lapansi. Mulungu atipatsa zambiri kutikondweretsa, zinthu zambiri zabwino! Koma kupita Kumwamba ndi kukhala ndi Yesu kudzakhala kwabwino kuposa kwambiri! Conco, sitiyenera kuopa kumwalira. Ngati ndife ana a Mulungu, tidzapita Kumwamba ndi kuona Mpulumutsi wathu wokondedwa. Tsiku lija lidzakhala lokondweretsa kwambiri!

**Kukambirana**
1. Kodi matupi a anthu a Mulungu adzasandulika bwanji?
2. Cifukwa ciani Paulo anati kuti kukhala ndi Kristu ndi kwabwino koposa?
3. Ndi ciani cimene ciri cabwino koposa kulingana ndi inu?
4. Kodi mulakalaka Yesu kubwera msanga?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu, Tidziwa Yesu ali kukonzekera kubweranso. Tsiku lija iri pafupi kwambiri. Tisintheni kuti tikhala ana anu obadwa mwatsopano, omvera ndi okonda kuti sitiyenera kumva mantha pa nthawi ya imfa yathu. Tithandizeni kusiya zoipa zonse. Tikupemphani izi zonse m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.

## 5. Kulemekeza Mulungu mpaka muyaya

*Taonani, ndidza msanga – Cibvumbulutso 22.12a*

**Kuwerenga**
Cibvumbulutso 21.1-7

**Malongosoledwe**
Kodi mukumbukira cifukwa ciani Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi? Inde, anazilenga kuti alemekezeke. Analenga zonse kuti alemekezedwe ndi kukhala wosangalala. Nyenyezi m'thambo, mbalame zoimba, maluwa: zonse ziyenera kumlemekeza Mulungu. Anthu nawonso. Onse azimlemekeza, pakuti Iye ndi Mulungu wamkulu ndi woyera, Mulungu amene analenga zonse, asamalira zonse ndi kutikonda.
Zonse zinalemekeza Mulungu paciyambi, uchimo usanafike kuononga cilengedwe cake codabwitsa. Ndipo tsiku lina zonse zidzamlemekezanso!
Baibulo litiuza za zinthu zodabwitsa zimene zidzacitika ndipo kenaka zonse zidzamtamandiranso ndi kulemekezanso Mulungu.
Pamene Yohane, m'modzi wa ophunzira a Yesu, anali mwamuna wokalamba, iye anatumidwa kutali ku cisumbu. Anthu oipa anamtuma kukhala kumeneko kuti iye sanakhoze kupitiriza kuuza anthu za Yesu.
Tsiku lina, pamene Yohane anali yekha, cinthu codabwitsa cinacitika. Yesu anadza kwa Iye. Yohane anaona Yesu: Yesu wakuwala ndi wolemekezeka monga ali Kumwamba tsono. Yohane anaona masomphenya. Cinali monga loto.
Yohane anagwada nkhope pansi pamene aona Yesu m'ulemerero wake wonse. Koma Yesu anaika dzanja lake pa Yohane nanena, 'Usaope. Ine ndi wamoyoyo ndipo ndinali kufa. Ndipo ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi'.
Kenaka Yesu anaonetsa Yohane zimene zidzacitika. Yohane analemba zonse m'buku. Tikhoza kuwerenga zonse za m'masomphenya ya Yohane m'buku lotsiriza m'Baibulo: buku lochedwa Cibvumbulutso.
Zinthu zina zimene Yohane anaona ziri zoopsa. Satana, anthu onse oipa ndi anthu amene sakonda ndi kutumikira Mulungu, analangidwa, komanso uchimo unalangidwa. Koma Yesu anaonetsa Yohane kuti zitapita zinthu izi zoopsa, kudzakhala zinthu zobweretsa ulemerero. Ndipo potsiriza, zonse zidzadzala ndi ulemerero wa Mulungu: mwamba komanso dziko lapansi!
Yohane anaona mwamba watsopano ndi dziko lapansi latsopano. Ndipo anaona mzinda wokongola wotsikira Kumwamba: mzinda watsopano wa Yerusalemu.
Kenaka Yohane anamva mau akuti, 'Onani, Mulungu ali kudza kukhala ndi anthu ake! Adzacotsa misozi yao yonse. Sikudzakhalanso cisoni, matenda, kuwawa kapena imfa!'
Yohane atiuza kuti anaona Yerusalemu watsopano wakuwala wa ulemerero wa Mulungu ndi wooneka bwino cifukwa ca miyala ya mtengo yapatali yenyezimira ndi yooneka bwino kwambiri. Ndipo mzindawo sunafunike kuwala kwa dzuwa kapena mwezi, pakuti Mulungu ndi Yesu ndiwo kuwala kwake. Ndipo sikudzakhala konse usiku. Kudzakhala cabe kuwala, cisangalalo, cimwemwe ndi kulemekeza Mulungu mpaka muyaya.
Pamene Yohane anaona izi zonse, iye anapempha, 'Bwerani, Ambuye Yesu!' Sanakhoze kuyembekeza zinthu zodabwitsa kucitika. Ndipo pamene ife tiganizira zodabwitsa zonse zimene zidzacitika ndiponso momwe tidzakhala m'ulemerero wa Mulungu, ifenso tipempha, 'Bwerani, Ambuye Yesu!'

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu adzacotsa ciani pamene Yesu abweranso?
2. Kodi anthu amene sanalandire Yesu kukhala Mpulumutsi wao, adzakhala kuti?
3. Kodi mumapempha Yesu kubwera msanga?
4. Kodi munalandira Yesu kukhala Mkhalapakati pakati pa Mulungu ndi inu kuti ndinu wokonzeka kukomana naye pamene abweranso?
5. Kodi mukumva bwanji za dziko lapansi latsopano? Lidzaoneka bwanji kulingana ndi inu?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Yesu, Tikupemphani kuti mutisandutse kuti ndife ana anu oona amene alakalaka kukhala pafupi ndi Inu m'ulemerero wanu. Bwerani msanga, Ambuye, cotsani zoipa zonse. Tikuyamikani kuti tsiku lina zonse zidzakulemekezani moonadi. Tikupemphani izi m'dzina lanu, Amen.